

ZOMBA URBAN DISTRICT MOCK EXAMINATION**2025 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE EXAMINATION**

CHICHEWA

(100 MARKS)

TSIKU : _____.

Subject Number:**Nthawi : 2 ¼ HRS****From: 12:00 – 2:15 PM****DZINA LANU** _____**(yambani ndi la bambo)****DZINA LA SUKULU YANU:** _____**MALANGIZO**

- Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi limodzi.
- Pepala ili lili ndi magawo anayi **A,B,C** ndi **D**.
- Lembani **dzina lanu** ndi **dzina la sukulu yanu** pamwamba pa tsamba lililonse.
- Lembani **nambala ya mayeso** pamwamba pa tsamba lililonse.
- Lembani **chimangirizo** kapena **kalata** mu Gawo **A** ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo **B,C** ndi **D**.
- Yankhani mafunso a mugawo **B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansu pa funso lilonse..
- Yankhani mafunso amu gawo **D** pozunguliza limbo lokhoza pafunso lililonse..
- Perekani pepala lanu kwa woyang'anira mayeso pamene mwauzidwa kuti mutero.
- Mu tebulo lomwe mwapatsidwali, chongani mafunso omwe mwayankha kupatula mafunso 6 mpaka 45.

Funso	Chongani zomwe mwayankha	Muno musalembemo	
1			
2			
3			
4			
5			
6- 10			
11-15			
16-20			
21-25			
26-30			
31-35			
36-40			
41-45			

Pitani kuseli

GAWO A (MALIKISI 30)

Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri omwe ali mmusiwa. Sankhani mutu wa chimangilizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo kapena kalata yanu asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu “MADZI OSEFUKIRA”

Mwazina tsatani izi polemba:

Ndime yoyamba

- Dera lomwe lidakhunzidwa ndi madzi osefukira
- Tsiku ndi nthawi yomwe madziwo adasefukira
- Komwe inu mudali panthawiyo

Ndime yachiwiri

- Zinthu zomwe zidaonongeka ndi madziwo
- Momwe dera lanu lidakhuzidwira ndi madziwo.

Ndime yachitatu

- Chithandizo chomwe mudalandira potsatira kusefukira kwa madziwo.
- Zomwe mukuchita ku dera lanulo pofuna kupewa kusefukira kwa madziwo.

KAPENA

2. Lemabni kalata kwa mzanu yemwe amakhala kunja kwa dziko lino

yomufotokozera za chisankho cha mtsogoleri wa dziko, aphungu a nyumba ya malamulo komanso makhansala chomwe chichitike mdziko muno cha chino.

Mwa zina tsatani izi polemba

Ndime yoyamba

- Cholinga cha kalata
- Tchulani tsiku, mwezi ndi chaka chomwe chisankhochi chidzachitike
- Amene ayenera kuzavota ndi ndani?

Ndime yachiwiri

- Tchulani zina mwa zipani ndi atsogoleri ake omwe aku zapikitsana.
- Tchulani ena mwa mavuto omwe anthu amakumana nawo pa nthawi yokonzekera chisankho.

Ndime yachitatu

- Atsogoleri a zipani, a mipingo ndi a mabungwe ena akuchitapo chiyani poonetsetsa kuti chisankho chizakhale cha mtendere.

GAWO B KUMVETSA NKHANI (MALIKISI 20)

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatirawa.

NAMAGETSI ANONG'ONEZA BONDO

Kunali chakummawa wa tsiku loweruka pomwe mnyamata wina dzina lake Maliko ankaperekeza wokondedwa wake Namagetsi kumalo okwerera basi a Mbongozi. Panthawi imeneyi n'kuti misozi yothamanga ndi yotentha ngati madzi ikutsikira mmasaya mwa mnyamatayo. Kumeneko kudali kulira polingalira kuti wachikondi wakeyo amachoka kupita kukagwira ntchito ku Lilongwe.

Basi yomwe adakwera Namagetsi isanafike, Maliko ndi wokondedwa wakeyo adali akucheza. Maliko adamuza wokondedwa wakeyo kuti chikondi chake sichizasintha ngakhale atakumana ndi mikwingwirima yotani. Adamukumbutsatso kuti kunja kuno kwaopsa choncho nkofunika kusamala. Ngakhale mnyamatayo adafotokoza zonsezi, kudali kungotaya nthawi chifukwa kwa njoleyo zinkangotulukira mbali ina ya khutu. Zooni zenizeni zidali zakuti Namagetsi sankamukonda Maliko chifukwa adali mphemvu m'dyera kunthiko, kwakwatuke wachabechabe.

Atayamba ntchito ija, mtima wake udaloza kwa njonda ina yomwe idali yokhupuka. Sipadatenge nthawi yaitali. Namagetsi adamutsiya Maliko uja ndipo adakwatiwa ndi njonda ija ngakhale idali ndi mkazi wina kale. Makolo a namagetsi adayetsa kumuletsa koma poti mwana akalilira nyanga ya nsatsi msemere imfotere yekha, adangomutsiya patangopita nthawi, namagetsi adapezeka kuti ali ndi pathupi. Atapita kusikero ya amayi oyembekezera kuchipatala, adamuyeza ndipo adamupeza kuti ali ndi kachilombo koyambitsa edzi ka HIV. Pamenepa adakumbukira malangizo a bwezi lake Maliko koma poti madzi akatayika sawoleka, iye adalira ndi kunong'oneza bondo.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.



- a. Kodi pakati pa Namagetsi ndi Maliko padali ubale wotani? _____ (Malikisi 1)
- b. Kodi malo amene adakwerera basi namagetsi ankawatchulidwa chani? _____ (Malikisi 1)
- c. Nchifukwa chiyani misozi ya Maliko inkasikira mmasaya? _____ (malikisi 2)
- d. Nchifukwa chiyani namagetsi adapita ku Lilongwe? _____ (Malikisi 1)
- e. Kodi Namagetsi ankafuna mwamuna wotani? _____ (Malikisi 1)
- f. Nchifukwa chiyani makolo a Namagetsi ankamuletsa kukwatiwa kwa njonda ija? _____ (Malikisi 2)
- g. Perekani zining'a kuchokera mnkhani zomwe matanthauzo ake ndi awa.
 (i). Mkazi wokongola _____ (Malikisi 1)
 (ii) Mavuto _____ (Malikisi 1)
- h. Perekani tanthauzo la mkuluwiko uwu kuchokera mkhoni :
isunge khosi kuti mkanda woyera idzavale.
 _____ (Malikisi 2)
- i. Fotokozani chifukwa chimene namagetsi adanong'oneza bondo. _____ (Malikisi 2)
- j. Kodi matenda a Edzi ngoopsa bwanji? _____ (Malikisi 1)
- k. Pezani mawu ofanana m' matanthauzo ndi otsatirawa kuchokera mu nkhanayi.
 (i). Pakati _____
 (ii). Yokhupuka _____
 (iii). Polingalira _____ (Malikisi 3)
- l. Perekani phunziro lomwe mwatengapo mu nkhanayi? _____ (Malikisi 2)

GAWO C (MALIKISI 10)

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

“Umboni wa mbali ziwiri taumva ndipo tonse tili ndi chithunzithunzi cha nkhanayi. Ndikukuuza kuti ine pogwira ntchitoyi sindiyang'ana nkhope. Ndiliba madyera mphoto m'pang'ono pomwe. Ndichitanso machawi popeza muvi woyang'anira suchedwa kulowa m'maso”

MAFUNSO.

- a. (i). Ndi malonje anji amenewa? _____ (1 Malikisi)
- (ii). Ndindani akuyankhula mmalonjewa? _____ (1 Malikisi)
- (iii). Mawu woti madyeramphoto akutanthauzani? _____ (1 Malikisi)
- (iv). Kodi mungasamalire bwanji pamalo omwe mumatunga madzi pasukulu yanu. Perekani njira

(v). Kodi zovala zakuda zimatanthauzanji kuno ku Malawi?

5. KUPANGA ZIGANIZO.

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

- (i). zingati _____
- (ii). obiriwira _____
- (iii). pokhapokha _____
- (iv). dowe _____
- (v). ku _____

GAWO D. (Malikisi 40)

Zungulizani lembo lokhoza A,B,C kapena D mmfunso otsatirawa.

Mafunso 6 – 10 Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kusi kwawo mziganizo zotsatirazi

- 6. Mtondo ndizabwera kwanu.
A. Dzina C. Muonjezi
B. Mfotokozi D. Mfotokozi
- 7. Kudya za masamba ndi kwabwino.
A. Mneni C. Muonezi
B. Dzina D. Mfotokozi
- 8. Aja alephera mayeso
A. Mlowammalo C. Mperekezi
B. Mfoto D. Muonjezi
- 9. Atupele watenga kanthu kanu.
A. Mlowammalo C. Muonjezi
B. Mfotokozi D. Mneni
- 10. Chikwakwa ndi chodulira udzu.
A. Mperekezi C. Mlumikizi
B. Mlowammalo D. Mneni

Mafunso 11 – 15 Sankhani ziganizo zomwe zili ndi zizindikiro zamkalembedwe zoyenera mziganizo zotsatirazi.

- 11. A. Mwana wanga, Elia uzilimbikira sukulu.
B. Mwana wanga, Elia, uzilimbikira sukulu.
C. Mwana wanga Elia uzilimbikira sukulu.
D. “Mwana wanga Elia uzilimbikira sukulu.”
- 12. A. Mbale, zili mbwe pabwalo.
B. Mbale zili mbwe pabwalo.
C. Mbale zili mbwe! Pabwalo.
D. Mbale zili mbwe, pabwalo.

- 13. A. Tawina adati, “galimoto yanga yasowa”
B. Tawina adati, “galimoto” yanga yasowa.
C. Tawina adati, Galimoto yanga yasowa.
D. Tawina adati, “Galimoto yanga yasowa.”

- 14. A. Kodi mwaphunzira?
B. Kodi? mwaphunzira.
C. Kodi mwaphunzira!
D. Kodi, mwaphunzira.

- 15. A. Chifukwa cha njala, iye adamwa zakumwa zonse?
B. Chifukwa cha njala? iye adamwa zakumwa zonse
C. Chifukwa cha njala, iye adamwa zakumwa zonse
D. Chifukwa, cha njala iye, adamwa zakumwa zonse.

Mafunso 16 – 20 Sankhani misintho ya aneni omwe atsekedwa mzere kusi kwawo.

- 16. Atsikana amagonagona akatopa
A. Wochitirana C. Wobwerezabwereza
B. Wochititsa D. Wotsutsa
- 17. Chisomo wabetsa ndalama zonse.
A. Wochititsa C. Wapoyera
B. Wochititsitsa D. Wonyazitsa
- 18. Mwana wamasula chingwe chija.
A. Wochititsa C. Wachibisira
B. Wochititsitsa D. Wotsutsa
- 19. Mphatso wapandwa ndi bambo ake.
A. Wonyazitsa C. Wotsutsa
B. Womchitira D. Wochitirana
- 20. Nyumbayi yamangika bwino
A. Wopoyera C. Womchitira
B. Wachibitsira D. Wonyazitsa

Mafunso 21 – 25 Sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa kungsi kwawo mziganizozo.

21. Kalulu uja wathawa.

- A. Li -, Ma- C. Ka-, Ti-
B. Mu-, A - D. I-, Zi-

22. Dzanja langa latupa

- A. Li-, Ma- Ka -, Ti-
B. Mu-, A- I -, Zi-

23. Agogo agula chikwama chokongola.

- A. Li-, Ma- C. I-, Zi-
B. Mu -, A- D. Chi-, Zi-

24. Mbalame yakondwa pa ulimbo.

- A. Mu-, A- C. I-, Zi-
B. Chi -, zi- D. U -, Ma-

25. Yohane wapita kumunda.

- A. Mu-, Mi- C. Ku-, Pa-, Mu-
B. Li-, Ma- D. I-, Zi-

Mafunso 26 – 30 Sankhani matanthauzo a zining'a zotsatirazi.

26. Atsikanawo ndi a mkamwa moola.

- A. Wochenjera C. Wotukwana
B. Wofatsa D. Woledzera

27. Achimwene awa ndi chulu cha ndiwo.

- A. Wokuba C. Wochenjera
B. Wopusa D. Wosokoneza

28. Tchalosi ndi wothothoka msidze

- A. Wokuba C. Wosokoneza
B. Wochenjera D. Wopanda manyazi

29. Amayi aja apita padera

- A. Abadwitsa mwana womwalira.
B. Ali ndi mwana wammuna
C. Apita kutawuni
D. Achira.

30. Mwanayu lero wauma m'maso.

- A. Ali ndi njala C. Wasowa tulo
B. Ndi ouma mutu D. Watupa maso.

Mafunso 31 – 33 Sankhani chachikazi cha izi

31. Phungu.

- A. Mpongozi C. Nankungwi
B. Zakhali D. Mfumakazi

32. Mphulu

- A. Mzambwe C. Nkhunda
B. Nkhosa D. Thadzi

33. Chipsolopsolo

- A. Msoti C. Mkota
B. Nkhosa D. Thadzi

Mafunso 34 – 35 Sankhani chachikulu cha izi

34. Kasawala

- A. Chitete C. Chambo
B. Mbewa D. Chule

35. Mbululu

- A. Mbuzi C. Chambo
B. Chule D. Mkulumutu

Mafunso 36 – 40 Sankhani matanthauzo awiri a mawu otsatirawa.

36. Chilere

- i. Munda wa mtedza
ii. Chiteme
iii. Munda wa chimanga
iv. Chisamale
A. i ndi iii C. ii ndi iv
B. i ndi iv D. i, ii ndi iii

37. Bala

- i. Chilonda
ii. Malo omwera mowa
iii. Bereka mwana
iv. Chipatso
A. ii ndi iii C. iii ndi iv
B. i ndi iv D. ii ndi iv

38. Khoma

- i. Chipupa iii. Chikhome
ii. Chimenye iv. Chipanda
A. ii ndi iv C. i ndi ii
B. i ndi iii D. ii ndi iv

39. Tsala

- i. malo olimidwa
ii. dzina la mtsikana
iii. usapite
iv. malo otsalimidwa
A. iii ndi iv C. i ndi iii
B. ii ndi iv D. i ndi ii

40. Chipanda

- i. Cholasa
ii. chipupa
iii. Chikhala kuti palibe
iv. Kumulanda chinthu
A. i ndi ii C. iii ndi iv
B. i ndi iii D. ii ndi iv



Mafunso 41 mpaka 45 Sankhani mitundu ya nthambi zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kungsi kwawo mziganzozo.

41. Sizachilendo zoti amadyera nyama.
A. Yamuonjezi C. Yadzina
B. Ya mfotokozi D. Yoima payokha
42. Zisanu zomwe zasowa ndi zanga.
A. Yamfotokozi C. Yamuonjezi
B. Yadzina D. Yoima payokha

43. Ana akusewera apowo ndi akuba
A. Yadzina C. Yamuonjezi
B. Yoima payokha D. Yamfotokozi

44. Amayi adafika titatha kudya msima
A. Yadzina C. Yamuonjezi
B. Yoyima payokha D. Yamfotokozi

45. Ife tidawaona pomwe amatuluka mnyumba
A. Yamfotokozi C. Yamuonjezi
B. Yadzina D. Yoima payokha

MAFUNSO ATHERA APA

